-Ngakhale kuti Yesu ankawoneka ngati ana ena onse, kodi Yesu ankasiyana bwanji ndi ana enawo?

-Yesu anali Mulungu.
-Yesu anali Mulungu weniweni komanso mundu weniweni.

-Yesu anakura ndikukhala munthu wa mzeru.

-Yesu anali ndi mzeru kwambiri ngati m'mene analonjezera Mulungu kudzera mwa aneneri kalekale.

-Yesu anadzadzidwa ndi Mzimu Woyera ngati m'mene analonjezera Mulungu kudzera mwa aneneri kalekale.

-Mulungu anasunga malonjezo ache.

-Mulungu saphwanya malonjezo ache



PHUNZIRO LA 47

1. Kodi Yesu anabadwira mu mzinda wanji?
-Mu mzinda wa Betelehemu ku Isirayeli.

2. Kodi Mulungu anakwiya chifukwa chakuti amuna amzeru anamupembedza Yesu?
-Iyayi.

3. Kodi chifukwa chiyani Mulungu sanakwiye chifukwa chakuti amuna amzeru aja anamupembedza Yesu?
-Chifukwa chakuti Yesu ndi Mulungu.

4. Kodi mngero wa Mulungu anamuwuza Yosefe kuti aŵatengere ku dziko liti Mariya ndi Yesu kuti mfumu Herodi isamuphe Yesu?
-Ku Iguputo.

5. Kodi ndani amene anamupatsa Herodi maganizo ofuna kumupha Yesu?
-Satana.

6. Kodi chifukwa chiyani Satana ankafuna kumupha Yesu?
-Chifukwa chakuti Satana sankafuna kuti Yesu aŵapulumutse anthu ku mphamvu ya tchimo, imfa ndi Satana.

7. Kodi chifukwa chiyani Mulungu anamuteteza Yesu?
-Chifukwa chakuti Mulungu anamutuma Yesu kuti aŵapulumutse anthu ku mphamvu ya tchimo, imfa ndi Satana.
-Chifukwa chakuti Mulungu anamuteteza Yesu, Iye anakula kukhala mnyamata wamphamvu.

Tiyeni tiŵerenge Luka 2:40

40-Mwanayo anakula ndipo anali wamphamvu, wa mzimu wamphamvu ndiponso wamzeru; madalitso a Mulungu anali pa Iye.

-Kodi Yesu sanamumvereko Mulungu
-Iyayi.

-Kodi Yesu anachimwako?
-Iyayi.

-Yesu anamvera lamulo lina lililonse la Mulungu, ndiponso sanachimwe.

-Kodi chifukwa chiyani Yesu anamvera lamulo lina lililonse la Mulungu, ndiponso sanachimwe?
-Chifukwa chakuti Yesu sanabadwire mu tchimo.

-Kodi chifukwa chiyani Yesu sanabadwire mu tchimo?
-Chifukwa chakuti Yesu analibe mbewu ya bambo wa umunthu.
-Chifukwa chakuti Yesu analibe mbewu ya mayi wa umunthu.
-Chifukwa chakuti Yesu anali Mulungu.
-Chifukwa chakuti Yesu sanabadwe ngati mwana wa Adamu ndi Hava, Yesu sanabadwe ndi tchimo.
-Chifukwa chakuti Yesu sanabadwe ngati mwana wa Adamu ndi Hava, Yesu sanabadwe ali osiyana ndi Mulungu.

-Yesu anamvera bwinobwino lamulo lina lililonse la Mulungu.
-Yesu sanaganize china chilichonse chimene chili cholakwa.
-Yesu sanalankhure china chilichonse chimene chili cholakwa.
-Yesu sanachite china chilichonse chimene chili cholakwa.



kha.
-Zonse zimene ankalankhula Yesu zinali zabwino zokhazokha.
-Zonse zimene ankachita Yesu zinali zabwino zokhazokha.

-Kodi Yosefe ndi Mariya anamvetsetsa zimene analankhula Yesu?

Tiyeni tiŵerenge Luka 2:50

50-Koma sanaŵadziŵe matanthawuzo a mawu ache amene anaŵayankhawo.

-Yosefe ndi Mariya sanazimvetsetse zimene analankhula Yesu.

-Yosefe ndi Mariya sanazimvetsetse zimene ankalankhula Yesu za Mulungu Atate.

-Atatha kulankhulana, Yosefe, Mariya ndi Yesu anabwelera kwawo ku Nazareti.

Tiyeni tiŵerenge Luka 2:51-52

51-Mnyamatayo pamodzi ndi makolo ache anabwelera kwawo ku Nazareti, ndipo anaŵamvera makolo ache; chomcho mayi ache anazisunga mu mtima mwawo zinthu zonsezi.
52-Mzeru za Yesu zimkakura kwambiri, msinkhu wache nawonso umkakula mu chikondi cha Mlungu ndi anthu.

-Yesu ankamumvera Yosefe ndi Mariya pamene ankakura.

-Kodi Mariya analankhula chiyani kwa Yesu pamene ana-mupeza Iye ali Mkachisi wa Mulungu?

Tiyeni tiŵerenge Luka 2:48

48-Makolo ache anadabwa kwambiri atamuwona Yesu; ndipo mayi ache anati kwa Iye, "Mwana wanga, kodi chifukwa chiyani wapanga zimenezi kwa ife? Tawona, ine pamodzi ndi bambo ako timakufunafuna ndipo ti-madandawula kwambiri."

-Kodi Yesu anayankha chiyani kwa Mariya?

Tiyeni tiŵerenge Luka 2:49

49-Ndipo Iye anati kwa iwowo, "Kodi chifukwa chi-yani mukundifunafuna Ine? Simumadziŵa kuti ndiyenera kupezeka M'nyumba ya Atate Anga a Kumwamba?"

-Kodi Mariya atamufunsa Yesu, Yesu anayankha chiyani?
-Yesu anati, "Kodi simumadziŵa kuti ndiyenera kupezeka Mnyumba ya Atate Anga a kumwamba?

-Kodi Yesu ankatanthawuza chiyani?

-Yesu ankatanthawuza kuti Iye ankachita zimene Mulungu Atate ankafuna kuti Iye adzichita.

-Yesu anali ndi zaka 12 zokha koma Iye ankamudziŵa Mulungu Atate.

-Yesu anamvera zonse zimene Mulungu Atate anamula-mura kuti achite.

-Zonse zimene ankaganiza Yesu zinali zabwino zokhazo-



-Kodi pali munthu amene alibe tchimo ngati Yesu.
-Palibe.

-Anthu onse anabadwira mu tchimo.

-Tiyeni tiŵerenga nkhani ya Yesu pamene anali mnyama-ta.

Tiyeni tiŵerenge Luka 2:41

41-Ndipo makolo ache ankapita ku Yelusalemu cha-ka china chilichonse pa nthaŵi imene anthu ankakhala ndi nsonkhano okumbukira tsiku la pasaka.

-Chaka ndi chaka, Ayuda ankapita ku mzinda wa Yelusal-emu ku chikondwelero cha Pasaka.

-Chaka ndi chaka, bambo ndi mayi ache a Yesu, Yosefe ndi Mariya, ankapitanso ku Yelusalemu ku Chikondwelero cha Pasaka.

-Pamene Yesu anakwana zaka 12, Yosefe ndi Mariya anamutenga Yesu ndikupita naye ku Yelusalemu.

Tiyeni Tiŵerenge Luka 2:42

42-Pamene mwanayo anakwana zaka khumi ndi ziŵiri, onse atatu anapita ku Yelusalemu ku Chikondwele-ro cha Pasaka ngati m'mene ankachitira anthu nthaŵi zonse.

-Pamene chikondwelero cha Pasaka chinatha, Yosefe ndi Mariya anawuyamba ulendo obwelera kwawo ku Naz-areni.

-Koma Yosefe ndi Mariya anayenda mtunda wawutari

osamupeza Yesu.

Tiyeni tiŵerenge Luka 2:43-44

43-Pamene chikondwelero cha Pasaka chija chinatha, makolo ache akubwelera kwawo, mnyamata wotchedwa Yesuyo anamusiya ku Yelusalemu; makolo ache asakudziŵa.

44-Iwowo ankaganiza kuti anali naye limodzi mu khamu la anthulo, zotsatira zache ndi zakuti iwowo anayenda mtunda wa tsiku limodzi, ndipo anayamba kumufunafuna mwa abale awo ndi anansi awo.

-Kodi chifukwa chiyani Yosefe ndi Maliya sankatha kumupeza Yesu?
-Chifukwa chakuti Ayuda ambiri anapita ku chikondwelero cha Pasakacho, chomcho mjiramo munali anthu ambiri.

-Chifukwa chakuti munali anthu achiwembu ambiri mjiramo, anthu ankayenda m'ma khamu.

-Chifukwa chakuti kunali anthu ambiri, Yosefe ndi Mariya sanathe kumuwona Yesu.

-Chifukwa chakuti kunali anthu ambiri, Yosefe ndi Mariya ankaganiza kuti Yesu akuyenda ndi azimzache.

-Yosefe ndi Mariya atadziŵa kuti Yesu sanali ndi iwowo, kodi anachita chiyani?

Tiyeni tiŵerenge Luka 2:45

45-Ndipo atalephera kumuwona, iwowo anabwelera ku Yelusalemu kukamufunafuna.

-Yosefe ndi Mariya anabwelera ku Yerusalemu kukamufunafuna Yesu.



-Kodi Mariya ndi Yosefe anakamupeza kuti Yesu?

Tiyeni tiŵerenge Luka 2:46-47

46-Patatha masiku atatu, iwowo anamupeza Iye Mnyumba ya Mulungu (M'kachisi) atakhala pakati pa aphunzitsi, akumvera zimene ankaphunzitsa ndi kumaŵafunsa mafunso.

47-Ndipo onse amene ankamumvera Iye anadabwa ndi mzeru zache ndipo kuyankha kwache kwamzeru kwa mafunso.

-Yosefe ndi Mariya anamupeza Yesu ali M'kachisi wa Mulungu ku Yelusalemu.

-Kodi Yesu ankachita chiyani M'kachisi wa Mulungu?
-Yesu anakhala ndi aphunzitsi a malamulo amene ankaphunzitsa mawu a Mulungu.

-Yesu ankaŵamvera aphunzitsi a mawu a Mulungu akuphunzitsa komanso kumaŵafunsa mafunso.

-Yesu ankaphunzitsanso mawu a Mulungu kwa ophunzitsa mawu a Mulungu.

-Kodi Yesu ankaŵadziŵa bwanji mawu a Mulungu pamene Iye anali ndi zaka 12?
-Chifukwa chakuti Yesu anali Mulungu.

-Aphunzitsi a mawu a Mulungu anali odabwa kwambiri chifukwa chakuti Yesu ankaŵadziŵa kwambiri mawu a Mulungu.

-Iwowo sankadziŵa kuti Yesu anali Mulungu.